

KUPANGA KOMPOSITI

Ndondomeko yogwiritsa nchito alimi ang'onoang'ono

Kodi kompositi ndi chiyani?

Kompositi ndi fataleza wopangidwa kuchokera ku zinthu zomwe ziwola bwino bwino pamene pali mphweya wabwino. Zitsanzo za zinthu zimene zimawola ndi mayani, udzu, zokhalira za zokola ndi zina zotere.

Kodi nchiyani chimene chifunika kuti mupange kompositi?

- ▶ Zinthu zouma zimene zikhoza kuwola zitsanzo za zimenezi ndi udzu wouma, zokhalira za chimanga, mpunga ndi zina zotere.
- ▶ Msipu womwe ukhoza ku wola (ngati ndi wopezeka). Msipu ndi umene umapatsa zakudya ku tulombo tosaoneka ndi maso kuti tuyambe kuwolesa ndiponso kupanga mphweya wa nitrogen. Zitsanzo ndi mayani a tithonia, komfiri, gliricidia ndi zina zotere.
- ▶ Ndowe zochokera ku ziweto zosiyanasiyana zimene zitipatsa mphweya wa nitrogen ndiponso tizilombo tosaoneka ndi maso. Zitsanzo za ziweto komwe tingatenge ndowe ndi ng'ombe, mbuzi, nkukhu, nkumba, mbelele ndi zina zotere.
- ▶ Zina zofunika popanga kompositi ndi madzi, nthyonthyo ndi dothi ya pa chulu olo dothi lopezeka munsu mwa mitengo.

Tsatanetsatane wa njira yopangila kompositi



Sitepi 1. Takonzani malo pomwe mufuna kupangila kompositi yanu kugwiritsa nchito mphompho pama kona onse anayi.



Sitepi 2. Yalani nthyonthyo zanu pansu kuti zikhale posamira kompositi yanu ma sentimitala 25 kufika 30.



Sitepi 3. Ikani udzu kapena ma yani ouma pamwamba pa nthyonthyo ma sentimitala 20 ndipo thirani madzi okwanira kuti zomazi zifewe.



Sitepi 4. Yalani msipu ma sentimitala 10. (Kumbukani ngati msipu ndi wosapezeka makamaka nthawi za malanga, mungathe kujumphila stepi imeneyi).



Sitepi 5. Ikani ndowe pamwamba pa msipu ma sentimitala 5. Ngati ndowe ndi zouma, wazani madzi ku ndowe kuti zinyolowe ndi kufewa.



Sitepi 6. Ikani dothi yoyolewa munsu mwa mtengo kapena la pa chulu ma sentimitala pakati pa 2 ndi 3. Kumbukaninso kuti stepi iyi mungaichite ngati zimezi zipezeka kwanuko.



Sitepi 7. Ikaninso zofunika pa kompositi yanu mwa kubweza kuchokera sitepi 3 kufikira sitepi 6. Chitani zimenezi mpaka kompositi itafika utali wosapitilira pa ma mitala 1.5. Kumbukani kuika madzi nthawi zonse mutaika zouma.



Sitepi 8. Jinyani mutengo mu kompositi yanu paka kufika pansu kuti ukhale chopimira kupsa kapena kuzizira kwa kompositi yanu.




Sitepi 9. Kupindimula kompositi - Kupsa kwa kompositi ndikofunika kwambiri chifukwa ndi chidziwitso cha pomwe mufunika kupindimula kompositi yanu. Zinthu zonse zitayenda bwino, mungapindimule kompositi yanu patapita ma sabata awiri kapena atatu kuchokera pomwe munapangila kompositi.

Choonde chereani khutu: Mufunika kupindimula kompositi ngati mutengo ukali wozizira patapita sabata limodzi. Ichi chitanthauza kuti tizilombo tukalibe kuyamba kugwila nchito olo kapena tulombo tuli kugwira nchito pang'ono pang'ono. Ichi chingakhale chifukwa chakuti: (i) ndowe zinali zochepe; olo (ii) mnyontho ndi wa ung'ono kapena wa pakisa kwambiri.

Mwa njira iliyonse, kompositi ifunika ku pindimula kuti zimenezi zikonzedwe. Ngati zonse zofunikira mu kompositi zinaikidwa bwino, kompositi yanu ifunika kupsa mutapindimula kanayi olo patapita ma sabata 8. Nthawi zina kompositi imapsa kwambiri chifukwa ndowe inaikidwa yambiri. Zimenezi zikachitika, mufunika kupindimula kompositi ndi kuika udzu kapena mayani owuma.

Kuika madzi: Zindikirani kuti nthawi yabwino yoika madzi ndi pamene muyala kompositi yanu ndiponso po pindimula. Kuthira madzi mutapanga kale kompositi yanu, sicholedwa chifukwa madzi sakhoza kulowa kuti zopangila kompositi zinyolowe ndi kufewa bwino bwino.



Promotion of agroforestry

Supported by:



With support from



by decision of the German Bundestag

Prepared by: Daniel M. Kalala; Graphic design: Jonathan